NYA_TTB_0905_20160916_script

**Ezekieli : 38:1-39:7**

**Mutu : Kuonongeka kwa Israyeli ndi Gogi**

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero Ambuye atitsogoze ndi mau ake apa 1 Yohane 5:4, akuti, “Pakuti chiri chonse chabadwa mwa Mulungu chililaka dziko lapansi; ndipo ichi ndi chilakotililaka nacho dziko lapansi, ndicho chikhulupiriro chathu.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kukambira pa Ezekieli 36:35-37:28, pamene timakambirana nkhani ya chithunzi cha kuukakwa Israyeli. Ndipo lero tilowa mu Ezekieli 38:1-39:7, momwe tisanthula kuonongeka kwa Israyeli ndi Gogi.

**Ezekieli 38**

Chapter chino pamodzi ndi chotsatirachi, chikufotokonza za chiononongeko cha Gogi pamodzi ndi asirikari ake amphamvu. Koma pamene tikuona liwu lakuti Gogi, m’dziko la Magogi, ndifuna muone likufotokonza za Rosi, Meshech ndi Tuba kuti ndiwo amene akudza kudzathira nkhondo pa Israyeli amene wabwezeretsedwa ku dziko lake. Ndiye pamene tiona za tanthauzo la Rosi ndi Meshech,

komanso malo a kumpoto ndi maganizo amene ali munkhani imeneyi, tipeza kuti Rosi, Russia, amene likulu lake ndi Moscow, dzina lomwe likuimiridwa ndi Meshech. Pamene Tabul ndiyo njira yopita mu Siberia.

Tsono uwu, ndiwo mtundu wa anthu omwe unachokera kumpoto motsogozedwa ndi Mulungu, kukaononga Israyeli amene ali pa mtendere. Izi, zinali chomwechi chifukwa Mulungu anali ndi cholinga chakuti pamapeto ake, adzionetsere yekha ku mitundu ya anthu apa dziko lapansi kuti ndiye Yehova. Kunena kuti kudzera pa mapiri a Israeli Gogi ndi asirikali ake onse, adzagonjakudzanja kapena chilango cha Mulungu. Tsono pamene izi zidzachitika, mitundu ya anthu padziko lonse lapansi kuphatikiza Israeli, adzadziwa kuti chilango chinawagwera chifukwa cha uchimo wawo, popeza kale Mulungu anapereka Israyeli m'manja mwa adani ake, koma pano Mulungu yemweyo akunena kuti sadzatayewopulumutsidwa ake. Awa, ndiwo mau amene ali pa Ezekieli 38:21, amene akuti, "Ndipo ndidzamuitanira lupanga ku mapiri anga onse, ati Ambuye Yehova munthu ali yense lupanga lake lidzaombananalo la mbale wake."

1. Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti;
2. Wobadwa ndi munthu iwe, lozetsa nkhope yako kwa Gogi, wa ku dziko la Magogi, ndiye mfumu yaikuru ya Meseki ndi Tubala;

Dzina la Gogi, ndilo dzina la mfumu, lomwe Ezekieli walitchula kuchokera ku dziko, lomwe ali mfumu yake. Kutanthauza kuti ziri monga momwe Farao ali mfumu ya Aigupto.Tsono Ezekieli ndiye amene watumidwa kuti apereke Uthenga Gogi, mfumu yankhanza, kuti Mulungu akutsutsana naye. Ndiye nkhani iyi, ikuti Mulungu sakungoona anthu amene ali adani a Mpingo wake wokha, ndi kudana nawo, koma akuonanso kutsogolo kutari kumene anthu ena angakhalenso ndi mtima wodana ndi ana a Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, taonani kudzera mwa mau amenewa kuti Mulungu ndiye wamtimawachifundo, amene amatonthozeratu ana ake, ngakhale pamene mabvuto asanadze, Iye amawauziratu kuti zonse ndizotheka ndi Iye.

3. Nuneneremotsutsana naye, uziti atero Ambuye Yehova, taona, nditsutsananawe, Gogi iwe, mfumu yaikuru ya Meseki ndi Tubala;

Mau awa, akunenedwa mobwereza-bwereza ndi cholinga chakuti pali chitsimikizo chonse chakuti Ambuye, Mulungu Wamphamvuyonse, amene ali Mfumu ya mafumu, adzamutaya kunja kotero kuti mayina aulemuakuitanira, sadzakhoza kumulanditsa iye.

Tsono nkhani ikunena kuti Mulungu ndiye amene akuyitanitsaGogi kupita ku Israeli kuti akaononge, koma pali cholinga chakuti Mulunguyo akadzionetsere yekha ukulu ndi ulemerero wake pakupereka chilango pa Gogi uja.

4. Ndipo ndidzakutembenuza ndi kukowam'chibwano mwako ndi zokowera, ndi kukuturutsa ndi nkhondo yako yonse, akavalo ndi apakavaloobvalamokwaniraonsewo, msonkhano waukuru ndi zikopa zochinjiriza, onsewoogwira bwino malupanga;

Pano tikuona mfumu yankhazayi (Gogi), kuti ndiye akufanizidwa kuti ndi chirombo cha nkhanza, chomwe chikuumirizidwa kutsatira Mbuye wake. Mau awa ndi amene akufanana ndi amene analembedwa pa Yesaya 37:29, amene akuti, "Chifukwa cha kundikwiyira Ine kwako, ndi popeza kudzikweza kwakokwafikam'makutu mwanga. Ine, ndidzaikambedza yanga

m'mphuno mwako ndi chapakamwa changa m'milomo mwako, ndipo ndidzakubweza iwe m'njira yomwe unadzerayo."Ili, ndilo ganizo lomwe likuti Gogi, adzaumirizidwa ndi mphamvu ya Mulungu kumuturutsa m'dziko lake leni-leni. Awa, ndiwo mau adanena Mulungu pa Chibvumbulutso 20:8, amene akuti, "Nadzaturukakudzasokeretsa amitundu ali mu ngondya zinayi za dziko, Gogi ndi Magogikudzawasonkhanitsa achita nkhondo: chiwerengero chawo cha iwo amene chikhala ngati mchenga wa kunyanja."

Tsono ichi, ndicho chithunzi cha satana kuti ndiye amene amanyengerera mitundu ya padziko, koma Ezekieli ndiye akuonetsa ukulu wa Mulungu kuti ndiwo umalamuliro zochitika zonse ngakhale zoipa. Tere iyi, ndiyo nkhani yomwe ikupezeka pa 2 Samueli 24:1, yomwe ikuti, "Ndipo mkwiyo wa Yehova unayakanso pa Israyeli, nafulumiza Davide pa iwo, nati, mukanuwerenge Israyeli ndi Yuda." Nkhani ikuti Mulungu adzagwiritsa ntchito chirombochoopsachi, chimene chidzaganiza kuti chikuchita maganizo ndi chifuniro chake, koma pamene chikutumikira Mphamvu ya wam'Mwamba, yomwe idzathera m'chionongeko

chake. Mwanjira ina tikunena kuti satana mwa mphamvu ya Mulungu, adzaloledwakunyenga anthu, koma akupita ku chiononongeko chake. Awa, ndimau amene akupezeka pa Chibvumbulutso 20:7-8, amene akuti, “Ndipo pamene zidzatha zaka chikwi, adzamasulidwa satana m’ndende yake; nadzaturukakudzasokeretsa amitundu ali mu ngondya zinayi za dziko, Gogi ndi Magogi, kudzawasonkhanitsa achita nkhondo.” Koma pali cholinga chakuti Yehova amuononge pamodzi ndi ana ake omwe, monga mwa mau apa Ezekieli 29:4, pamene akuti, “Koma ndidzaikambedza mkamwa mwako, ndi kumamatiritsansomba za m’mitsinje mwako, ku mamba ako; ndipo ndikukwezakukuturutsa mkati mwa mitsinje yako, pamodzi ndi nsomba zonse zomamatira pa mamba ako.” Mwa mau amenewa Mulungu akunena kuti adzagwiritsa ntchito Gogi, kuti achoke m’dziko mwake ndi kukathira nkhondo mu Yudeya, monga muja Yehova adanyengereraSisera ndi gulu lake, pamene tiwerenga Oweruza 4:7, pamene Mulungu akunena kuti, “Ndipo ndidzamkokaSisera, kazembe wa nkhondo ya Yabini, ndi magareta ake, ndi aunyinji ake; ndipo ndidzampereka m’dzanja lako.”

8. Atapita masiku ambiri udzakumbukirika; zaka zotsirizaudzalowa m'dziko lobwezedwalopulumuka lupanga, losonkhanidwalituruke m'mitundu yambiri ya anthu, pa mapiri a Israyeli, amene adakhalaachipululu chikhalire; koma liturutsidwa m'mitundu ya anthu, ndipo adzakhala mosatekesekaonsewo.

Tsono pamene Gogi, anali kukokedwa ndi mphamvu ya Yehova kuti akathire nkhondo pa Israyeli, panali cholinga chakuti Gogiyoakaonongekere pomwepo.Tere, chikonzekero chomwe akuchita Gogi, ndiyo ndime yoyamba pakumdzera mphamvu ya Yehova. Ichi, ndichimene akutanthauza kuti Gogi ayenera kukwera ku mapiri a Israyeli, amene anakhala chipululu kwa nthawi yaitari, koma pano anthu anakhalamo. Mwanjira ina ichi, ndichithunzi cha Ufumu wa Mesiya, chomwe chikutsimikizakukhazikika kwa Ufumu wa Mulungu, umene udzakhala nthawi yamuyaya. Mau awa, akufanana ndi mau omwe adanenedwa pa Genesis 49:1, pamene Yakobo akunenakuti, “Sonkhanani inu, kuti ndikuuzeni inu chimene chidzakugwerani inu masiku akudzawo.” Apa, anali kunena m'masiku amtsogolo m'nthawi ya Ufumu wa Mulungu.

Ndiye kugwa kwa Gogi, ndiko kumene kudzachitititsakuthekera kuti a Yuda, amene ndi eni ake a dzikoli, adzasonkhanitsidwa, kuchokera ku maiko komwe anathawira, ndi kukhala m'dziko lawo mwamtendere, osaopanso kanthu kena. Uku, ndikuperekabe chithunzi cha momwe zinthu zidzakhalira mu Ufumu wa Kristu, womwe ukudza ndi kubwera kwake kwachiwiri.

16. Ndipo udzakwerera anthu anga Israyeli ngati mtambo wakuphimba dziko; kudzachitika masiku otsiriza ndidzabweranaweulimbanenalo dziko langa, kuti amitundu andidziwe, pozindikiridwa Ine woyera mwa iwe, Gogi, pamaso pawo.

Mulungu pano akuuzaGogi, mfumu yankhazamobwereza kuti adzakwerakukathira nkhondo Israeli, kutsimikiza kuti zidzachitikadi.Kutanthauza kuti Gogi, adzathira nkhondo osati kuti iye akapezemo ulemu ndi mtendere ayi, koma ndi cholinga chakuti akaonongekemo. Komanso osati pakakhalepoopsezera Israyeli ayi, koma kuti ulemerero wa Mulungu ukaonekere.

Ndiye pamene atchula zakuti Gogiadzakwerera Israyeli ngati mtambo, akukamba za kuchuluka kwa asirikari ake, amene

akathirenkhondoyo. Tsono nkhondo imeneyi, idzachitika pamene Israyeli adzabwererakudziko lawo monga mwa mau apa Hoseya 3:5, pamene Yehova akuti, “Atatero ana a Israyeli adzabwera, nadzafuna Yehova Mulungu wawo, ndi Davide mfumu yawo, nadzafika ndi mantha kwa Yehova, ndi kukoma kwa Yehova, ndi kukoma wake masiku otsiriza.”

Kutsimikiza kuti Mulungu ndiye adzalola nkhondo imeneyi kuti ithirike pa Israyeli ndi cholinga chosatichoononga dziko kaya anthu okhala m’menemo ayi, koma kuti maufumu achikunja monga a China ndi ena, adzafikepozindikira Mulungu woona ndikukhala iwo gawo limodzi la Ufumu wa Kristu. Ili, ndilo ganizo lomwe likupezeka pa Chibvumbulutso 11:15, pamene tipeza mau akuti, “Ndipo mngelo wachisanu ndi chiwiri anaombalipenga, ndipo panakhala mau akulum’Mwamba, ndi kunena Ufumu wa dziko lapansi wayamba kukhala wa Ambuye wathu ndi wa Kristu wake: ndipo adzachita ufumu kufikira nthawi za nthawi.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani yonseyi idzachitika ndi cholinga chakuti pakupereka chilango pa adani a anthu ake, ukulu ndi mphamvu zake zionetserekuti ndiye Woyera, Wolungama ndi

Wokhulupirika. Iyi, idzakhala njira imodzi yokwaniritsira ulosi wonse wokhudza Gogi ndi mitundu inayosadziwa Mulungu, kuti azindikire ukulu wa Mulungu, ndikuti Mulungu wa Israyeli, ndiye woona, Atate wa Ambuye wathu Yesu Kristu. Uyu, ndikristu amene ali Mesiya Mutu wa chikristu kuti iwonso (anthu akunja), akakhulupirire dzina lomweli. Kutsindika mau aja adanena Mulungu pa Eksodo 9:16, pomwe anauza Mose kuti, “Koma ndithu chifukwa chake ndakuimika kuti ndikuonetse mphamvu yanga, ndi kuti alalikire dzina langa pa dziko lonse lapansi.”Kutanthauza kuti Mulungu nthawi zina amalola kuti ana ake agwe m’masautso ndi kupsinjika ndi cholinga chakuti Iye alandira ulemu pakuwalanditsa. Zimachitika izi, pamene akhaulitsa adani a anthu ake ngakhale amanyasitsa dzina lake chifukwa cha uchimo wawo. Koma chuma chonsechi cha wokhulupirira ndicho chakhazikika m’mau a Mulungu, ngakhale mpingo ulikuzunzika komanso uli ndi masautso akulu.Kutanthauza kuti dzina la Mulungu ndilo liyeneradikumangirirapo chikhulupiriro cha wokhulupirira aliyense.Kodi inu munalikhulupirira kale Dzinali?

**Ezekieli 39**

Chapter chino chikupitiliza kuonetsa ulosi wotsutsana ndi Gogi komanso chikupereka mau otsindikaamomwe chiononongeko cha ankhondo ake olimba ndi amphamvu, chinachitikira.

2. Ndipo ndidzakutembenuza ndi kukutsogolera ndi kukweza iwe uchoke ku malekezero a kumpoto; ndipo ndidzadzanawe kumapiri a Israyeli;

Pano Mulungu akunena kuti adzatsogoleraGogi, m’dziko lake ndi kuzungulira naye momwemo ndi kutsikirakudziko la Israeli.Apa, mukhoza kuonadi kuti inali mphamvu ya Mulungu kuti chikwaniritsidwe cholinga chake.  Kunena kuti panali cholinga chakuti pamene m’dani Wamkulu wa ana ake, adzaononongeka, ndipo pamene ulemu ndi ulemerero wa Mulungu udzaonekera. Taonani akunena kuti gawo lalikuru la asirikari a Gogi ndiwo amene adzakwera kumapiri a Israyeli, kusiya owerengeka, koma asirikari ochuluka aja, ndiwo amene akatha onse ndikupereka mantha ku asirikari ochepa otsala aja.  Kumene kuli kuthakwa ufumu wa Gogi, nthawi yomweyo dzina la Mulungu wa Israyeli lidzakwezeka.  Tere, tikuphunzira kuti ngakhale asirikali atame mphamvu, ukatswiri ndi zida zawo zamphamvu komanso

zochuluka, sizikwanirakugonjeza kapena kuletsa cholinga cha Mulungu.Ichi, ndichifukwa chake verse 3, likunena kuti, “Ndipo ndidzakanthauta wako, kuchotsa m’dzanja lako lamanzere, ndi kutayitsamibvi yako ku dzanja lako lamanja.”

Koma taonani kuti pamene Yehova anathana ndi m’dani Wamkulu wochokera kumpoto, amene anathira nkhondo pa Israeli, akulorawotsutsa Kristu kuti akhale wolamulira dziko lonse m’nthawi yachisautso chachikulu. Ndiye pakutha pa ulamuliro umenewu, ndipo pamene Ambuye Yesu Kristu adzadza ndi kukhazikitsa ufumu wake. Ichi, ndicho chithunzi chomwe tikuchiona m’chapter 19 ndi 20 cha buku la Chibvumbulutso.

6. Ndipo ndidzatumizira moto Magogi, ndi iwo okhala mosatekesekam’zisumbu; moteroadzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

Poyamba pano ndifuna muone kuti Gogi, ali m’dziko la Israyeli, pamodzi ndi nkhondo yake yonse. Ndipo ali m’menemo iye ndi asirikari ake onse apululuka, dziko lakensolayatsidwa moto. Koma ndime ino, ikusonyeza kuti chilango cha Gogisichifikira iye yekha ndi dziko lake ayi, komanso zisumbu zomwe ziri ndi maganizo

ofanana ndi Gogi, oukira ndi kudana ndi ufumu wa Mulungu. Kutanthauza kuti analipo anthu ena amene amakhala m'zisumbu, ndipo anali kuthandiziraGogi ndi zida za nkhondo.Iwowa, anali kukhala mwamtambasale, kunena kuti anali kukhala mopanda nkhawa ndi moyo wawo.  Komanso, ndimeyi ikutiasirikari pamodzi ndi anthu onsenawonsoadzalandira moto waukali wa Mulungu m'dziko lawo lomwelo.Tere, chilango ichi, ndichimene chidzaonetsa kuti wachita ndi Mulungu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, phunziro pano likunena kuti anthu amene amakonda kuononga ufulu wa anthu ena, nawonsomwachilungamo cha Mulungu, amataya ufulu wawonso. Apa, ndipo pamene Mulungu amaonetserakukula kwa dzina lake. Taonani poyamba anthu ake, Israyeli adzazindikira zambiri za dzina la Yehova, kotero kuti iwo amene adzadziwadichiyero cha dzina la Mulungu sayerekeza kunyazitsa dzinalo.

Kachiwiri, tiona kuti anthu amene sadziwa Mulungu, adzamudziwa ndi dipo lalikuru pamene amatsimikiza kuti ndiye Mulungu, amene safuna kukangana naye.Kutsimikiza kuti palibe ndi munthu

m'modzi yemwe anakangana ndi Mulungu anapulumuka.Kodi inu mufunakuyesera kukangana naye?

7. Ndipo ndidzadziwikitsa dzina langa loyera pakati pa anthu anga Israyeli, osalola dzina langa loyeraliipsenso; ndipo amitundu adzadziwa kuti Ine ndine Yehova Woyerayowa Israyeli.

Iyi, ndi ndime yomwe ikufotokonza kuti Mulungu sakufuna kuti anthu akunja anyazitse dzina lake monga poyamba paja anali kunena kuti, Mulungu analephera kapena kuti samafuna kupulumutsa anthu ake, kuchoka m'dzanja la m'dani wake Wamkulu.Koma pamene aona chilango chimenechi, asowachonena ndipo kuti sadzapitilizakunenera mwano dzina la Yehova. Nthawi yomweyo a Israyeli nawonsoadzafulumizidwapakuona chisomo ndi kukoma mtima kwa Mulungu, komwe kunadza pa iwo, sangayerekeze kugwa pauchimomwadala monga momwe anali kuchitira kale. Mwanjira imeneyi, dzina la Mulungu linali kunyozeka.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti Mulungu wa Israyeli ndiye Mulungu woona, kotero inu ndi ine,

tiyenera kumudziwa kuti ndiye woyera ndi wolungama. Uyu, ndiye Mulungu amene amaonetsa chisomo chake ndi kupezeka kwa mphamvu yake kwa anthu ake, pamene adani awo ayeserakuwazuza iwo. Mwanjira ina nkhani yonseyi ikutsimikiza mau apa Eksodo 14:13-14, amene amati, "Yehova adzakugwirirani nkhondo, ndipo inu mudzakhala chete." Kodi chifukwa chiyani mumachita mantha pamene Yehova alipo?

Lero tilekeza pano. Koma timasanthulaEzekieli 38:1-39:7, momwe timaona kuonongeka kwa Israyeli ndi Gogi.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!